# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## NTHAMBI YOONA ZA NYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO


## ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'BOMA LA CHIKWAWA, 2025-2026

## DZINJA LA 2025/2026 MWACHIDULE

Katenthedwe ka Nyanja ya mchere ya Pacific sikakhudza kwambiri nyengo ya dzinja ya 2025/26.

Boma la Chikwawa likuyembekeza kulandira mvula ya mlingo wokhazikika kapena yoposera apo mu nyengo ya dzinja la 2025/2026.


## October 2025




Madera ambiri akuyembekezeka kukhala opanda mvula mwezi wa October komabe mvula ya chizimalupsya ikhoza kuzagwa m'madera ena yosaposela 30mm.

Mvulayi ikhoza kukhala ya ziphaliwali komanso ya mphepo ya mkuntho


## November 2025




Mlingo wa mvula okhazikika kapena kuchepela apo okwanira 50-100mm ukuyembekezeka m'madera ambiri m'mweziwu.


Mvulayi idzatsatsagana ndi ziphaliwali komanso mphepo ya mkuntho

## December 2025




Madera ambiri akuyembekeza kuzalandira mvula yopyola mlingo wokhazikika yokwana 200-250mm m'bomali mwezi wa December 2025.
Madera ena monga a TA Ngabu, TA Lundu ndi Chikwawa boma adzalandira mlingo osaposera 150mm.
Mvula yokhazikika ikuyembekezeka kudzayamba sabata loyamba lamwezi uno.


## January 2026




Mvula yamlingo okhazikika kapena oposela apo yokwana 250mm ikuyembekezeka m'madera ambiri pamene madera ena a TA Ngabu, TA Katunga ndi TA Maseya akuyembekezeledwa kuzalandira mvula yosapyola 200mm.

Komabe pali kuthekera kwa ng'amba yofika masiku asanu ndi awiri m'madera ena


## February 2026




Mvula ikuyembekezeka ya mlingo okhazikika kapena kucheperapo m'madera ambiri m'bomali, wa pakati pa 150 ndi 200mm m'mwezi wa February 2026.


Komabe pali kuthekera kwa ng'amba yofika masiku asanu ndi awiri m'madera ena.

## March 2026




Mvula ya mlingo okhazikika kapena yoposera apo ya pakati pa 150mm ndi 200mm ikuyembekezeka kudzagwa m'madera ambiri m'bomali

## April 2026





Mlingo wa mvula wa pakati pa 50mm ndi 100mm umene ndi okhazikika kapena kupyola apo ukuyembekezeka kudzagwa m'bomali mwezi wa April 2026.

Dzinja likuyembekezeka kufika kumapeto sabata lachiwiri la mwezi umenewu.

*Mvula yokhazikika ikuyembekezeka kuyamba sabata loyamba la December 2025. Dzinja likuyembekezeka kufika kumapeto sabata lachiwiri la mwezi wa April. Dzinjali likuyembekezeka kukhala lotalika masiku 120 ndi 130.* Komabe pali kuthekera kwa ng'amba yofika masiku asanu ndi awiri miyezi ya January ndi February

*Ndondomeko ya kagwedwe ka mvula ili musimu:*

| NGABU | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 1.8 | 30.4 | 29.3 |
| NOV | 38.4 | 92.2 | 62.6 |
| DEC | 99.5 | 182.8 | 150.6 |
| JAN | 138.4 | 227.6 | 222.9 |
| FEB | 99.9 | 200.4 | 140.0 |
| MAR | 51.2 | 117.2 | 101.0 |
| APR | 22.2 | 47.5 | 89.5 |




**Ulosiwu udzasindikizidwanso mu mwezi wa December 2025**

**Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:**
The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw

Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku: